**Funso**:

As-Salam alaykum! Kodi munthu woti unadzichekera mankwala achikuda mosadziwa malamulo achisilamu, ndiye kutha kwa nthawi wazindikira kuti ndi haram, ungatani?

**Yankho**:

Kutamandidwa konse ndi kwa Allāh!

Choyamba, munthu azindikire kuti kuchekera mankhwala achikuda kumagwera mu zigawo ziwiri. Gawo loyamba lili pawiri: kudzera mu njira yoletsedwa yomwe ndi kupita kwa sing'anga, wamatalasimu, wamaula, mfiti kapena mlosi. Kapena kudzera mu njira yololedwa yomwe ndi kuchekeredwa ndi wodziwa zitsamba amene sakugwera mu gulu loyambalo.

Ngati munthu unadzichekera mankhwala amene unakatenga kwa anthu a gulu loyambalo, pamenepo ukuyenera kulapa kwa Allāh chifukwa unapita ku malo oletsedwa. Abī Hurayrah akufotokoza kuti Mtumiki wa Allāh (ﷺ) adati:[1]

مَنْ أَتَى سَاحِرًا، أَوْ كَاهِنًا، أَوْ عَرَّافًا، فَصَدَّقَهُ بِمَا يَقُولُ فَقَدْ بَرِئَ مِمَّا أُنْزِلَ عَلَى مُحَمَّدٍ صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ.

*Aliyense amene wapita kwa Mfiti, kapena Bimbi, kapena Wamaula kenako nakhulupirira zomwe wayankhula iyeyo; pamenepo basi wakanira mu zomwe zidavumbulutsidwa kwa Muhammad (ﷺ).*

Gawo lachiwiri ndi mtundu wa mankhwala omwe ukuchekeredwawo kuchokera kwa munthu wa gulu lachiwirilo. Mtundu woyamba ndi mankhwala amene ali oletsedwa monga: mankhwala a mwayi, mangolomera, odzitetezera ku ufiti ndi matsenga kapena mankhwala alionse omwe akugwera mu zoterezi.

Jābir Ibn 'Abdullāh akufotokoza kuti:[2]

سُئِلَ رَسُولُ اللَّهِ صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَسَلَّمَ عَنِ النُّشْرَةِ، فَقَالَ: هُوَ مِنْ عَمَلِ الشَّيْطَانِ.

[1] Musnad Ibn Al-Ja'd, #1951, Musnad Ahmad, #9288
[2] Sunan Abī Dāwūd, #3868

*Mtumiki wa Allāh (ﷺ) adafunsidwa zokhudza kupeza machiritso kudzera mu ufiti (An-Nushrah), choncho iye adati: "Imeneyo ndi imodzi mu ntchito za Shaytwān."*

Mtundu wachiwiri ndi mankhwala amene ali odziwika kuti Allāh adaikamo machilitso ndipo amachizadi nthenda imene ukufuna kuti uchireyo. Monga mankhwala a mutu wa ching'alang'ala, mankhwala a mphumu, ndi ena oterowo omwe munthu umathanso kuwapeza kudzera ku chipatala.